Khalani ndi Makhalidwe Amene Mulungu Amasangalala Nawo (Gawo 3)

Nkhaniyi yachokera m'mutu 12 wa buku lakuti, *Kodi Baibulo Limaphunzitsa Chiyani Kwenikweni?* lomwe likupezeka pa jw.org/ny.

ZIMENE MUYENERA KUCHITA: Ganizirani mofatsa zimene mumakhulupirira ndiponso zifukwa zake. Fufuzani zimene Baibulo limaphunzitsa, kenako ganizirani mmene mungafotokozere ena zimene mumakhulupirirazo.

KODI KUYESETSA KUCHITA ZINTHU ZOSANGALATSA MULUNGU N'KOTHANDIZA?

1 GANIZIRANI MOFATSA ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

N'chifukwa chiyani anthu ena angayankhe kuti, ayi?

N'chifukwa chiyani anthu ena angayankhe kuti, inde?

Kodi **inuyo** mumakhulupirira zotani?

Nanga n'chifukwa chiyani mumakhulupirira zimenezo?

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2 FUFUZANI ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA

Zimene Yehova amafuna kuti tizichita n’zothandiza ife tomwe komanso n’zosavuta kuzitsatira.
(Werengani mutu 12 m’buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 17 mpaka 19.)

Werengani Yesaya 48:17, 18.

Kodi zimene Yehova amafuna kuti tizichita zimatithandiza bwanji?

Werengani Deuteronomo 30:11-14 ndi Salimo 103:14.

Kodi mavesiwa akusonyeza bwanji kuti Yehova safuna kuti tizichita zimene sitingakwanitse?

Chovala chikada timachivula n’kuvala choyera. Mofanana ndi zimenezi tiyenera kuvula umunthu wathu wakale n’kuvala watsopano

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Tiyenera kuyesetsa kukhala ndi makhalidwe amene Mulungu amasangalala nawo.

(Werengani mutu 12 m'buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 20 mpaka 22.)

Werengani Aroma 12:9.

N'chifukwa chiyani sitifunikira kungopewa zimene Mulungu amadana nazo?

Werengani Akolose 3:9, 10.

Kodi tiyeneranso kuchita chiyani kuti tisangalatse Mulungu pambuyo poti 'tavula umunthu wakale'?

Kodi 'kuvala umunthu watsopano' kwakuthandizani bwanji?

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

3 FOTOKOZANI ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

WINA AKANENA KUTI…

N’zosatheka kuti munthu asinthe umunthu wake?

MUNGANENE KUTI…

Anthu ambiri akhoza kugwirizana ndi mfundo imeneyo. Koma ine ndimakhulupirira zosiyana ndi zimenezo chifukwa…

_____

_____

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Kodi mungafotokoze zotani kuti munthuyo amvetse bwino lembalo?

_____

WINA AKANENA KUTI…

Malamulo a Mulungu ndi opanikiza kwambiri.

MUNGANENE KUTI…

N’zoona kuti Mulungu anakhazikitsa malamulo oti tizitsatira. Koma ndimakhulupirira kuti malamulowa ndi othandiza chifukwa…

_____

_____

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Kodi mungafotokoze zotani kuti munthuyo amvetse bwino lembalo?

_____

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania